duducoelho.com

KODI CHOLAKWIKA NDI CHANI

NDI NDONDOMEKO YA KUKWEZA NTCHITO ZA MALIMIDWE MU AFRICA?

Ndondomeko ya Kukweza Ntchito za Malimidwe (Green Revolution) imakhudza ndi kuwongolela kwambiri Ndondomeko zoyendetsela ntchito za malimidwe za mu Africa, madongosolo komanso kayikidwe ka ndalama. Izi ndi zowonekelatu mu ndondomeko ndi mfundo za bungwe la mayiko amu Africa la African Union kutsikila ku ntchito ndi ma dongosolo a maboma komanso uphungu umene alangizi awo amapeleka kwa alimi.

Anthu ochepa chabe wochokela mgulu la anthu ochita bwino ndi amene amapindula kuchokela ku njira za Kukwaza Ntchito za Malimidwe:

- Alimi samakwanitsa kufikila maluso a mu ndondomekoyi, monga mbeu zamakono komanso mankhwala a za ulimi, kaamba ka kukwela kwa mitengo yake.
- Misika ya mbeu – kumene imapezeka – samakwanitsa kugula zokolola zowonjezeleka.
- Alimi ambiri amavutika kufikila milingo, kolite komanso zoyeneleza kuti agulitse mu misika ikuluikulu za zaulimi.
- Mitengo ya zokolola ndi yotsika kwambiri, makamaka pa nthawi ya kukolola, ndipo alimi osati kwawirikawiri amapanga phindu lochuluka kuchokela ku kugulitsa zokolola zowongezela.
- Ma banja amene amalima amasungako gawo lina la zokolola zawo ngati chakudya, koma kawirikawiri izi zimakhala za kolite yoyipa ndipo zimapangitsa kutsika mu mlingo wa ma madyedwe woyenelela.

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

african centre for biodiversity